MALANGIZO KWA ASILAMU PANTHAWI YA MULILI OMWE WAGWA MDZIKO LINO (APRIL 2020/SHABAN 1441 A.H)

Mau Oyamba

Ayamikike Allah Wapamwamba-mwamba ndipo madalitso ake ndi mtendere wake zikhale pa mthenga wake okondokea Muhammad (s.a.w) pamodzi ndi abale ake, ndi ophunzira ake ndi aliyense amene akutsatira njira yake kufikira tsiku la chimaliziro. Ndipo mtendere ukhale pa yemwe aatsate chiongoko!

Pambuyo pake;

Allah akuti: '…**ndipo musadziphe nokha (ngakhale kupha anzanu). Ndithu Allah ali Wachisoni pa inu**'. [Qur'an 4, Ayah 29]. Iye akuyankhulanso malo ena kuti: '…**ndiponso musadziponye ku chionongeko ndi manja anu**' [Qur'an 2, Ayah 195].

Ndipo Mtumiki (s.a.w) adati: '**Mthaweni munthu wakhathe ngati momwe mumauthawira mkango**'. [Bukhari]. Ndipo anthu ophunzira adati: '**Kupewa kuposa kuchiza**'. Enanso adati: '**Palibe chomwe chingafanane ndi kutetezeka (ku vuto)'**.

Udindo wa Msilamu aliyense **Page 02**
Mapemphero apagulu **Page 04**
Khalidwe la Msilamu weni-weni nthawi ya zovuta **Page 05**

1) UDINDO WA MSILAMU ALIYENSE

1.1. Mtumiki (s.a.w) adati: '**Aliyense wa inu ndi mdindo ndipo aliyense wa inu akafunsidwa za udindo wake**'. Chomwecho Msilamu aliyense ali ndi udindo otenga nawo gawo pothana ndi kufalikira kwa mulili omwe watipeza panthawi ino (komanso mlili ina iliyonse yomwe ingatipeze mu nthawi zina). Ndipo kunyalanyaza kutero ndikulakwira chiphunzitso cha Shari'ah yathu ndipo otero akafunsidwa pa tsiku la chimaliziro.

2.1. Msilamu aliyense akhale okhudzika ndi zomwe zikuchitika mdziko lake ndipo adziwe kuti kuteteza moyo wake ndi wa ena ku zoipa monga nthenda zofalikira, ndi udindo wa aliyense kuphatikizapo iye ngati Msilamu. Iye asakhale ngati ali dziko la yekha-yekha ayi, kutero sichilamu.

3.1. Msilamu aliyense ali ndi udindo oteteza moyo wake ndi wa anzake ku zoipa monga nthenda zofalikira ndi zina, ndipo akuletsedwa kudziyika dala iye mwini kapena anzake mchiwonogeko pozengereza kupewa. Allah akuti: '…**ndiponso musadziponye ndi manja anu ku chionongeko**'.

4.1. Msilamu aliyense adziwe kuti kuteteza moyo wa munthu mmodzi yekha ku chiwonongeko zili ngati wateteza miyoyo ya anthu onse kuyambira nthawi ya Adam (a.s) mpaka kutha kwa dziko. Chimodzi-modzinso kuwononga moyo wake kapena moyo wa munthu wina zili ngati waononga miyoyo ya anthu onse kuyambira nthawi ya Adam (a.s) mpaka kutha kwa dziko. [**Qur'an 5, Ayah 32**].

5.1. Msilamu ali ndi udindo oteteza dziko lake ndi dera lake ku chionongeko cha mtundu uliwonse. [**Qur'an 2, Ayah 205**]. Mtumiki (s.a.w) adati: '**E! Inu anthu! Falitsani (bata ndi) mtendere (pa dziko).** [Tirmidhi].

6.1. Msilamu ali ndi udindo owateteza asilamu anzake ndi anthu onse ku zoipa za manja ake, lilime lake (ndi zina zosiyana-siyana monga matenda ndi zina). Mtumiki (s.a.w) adati: '**Msilamu weni-weni ndi amene asilamu (anzake) amatetezeka ku (zoipa za) manja ake ndi lilime lake (ndi zina zotero)**. [Bukhari]. Adatinso: '**Okhulupirira weni-weni ndi amene anthu sakumuopa pa mwazi wawo ndi chuma chawo'**.

7.1. Msilamu aliyense ali ndi udindo otsatira ndi kugwiritsira ntchito njira zosiyana-siyana zodzitetezera ndi kudzichizira ku matenda monga kumwa mankhwala, kudzipatula kwa anthu odwala kuti asatenge matenda awo, kapena kudzipatula iye mwini kwa ena kuti asawapatsire matenda ake. Ndipo kulephera kutero ndi mbali imodzi ya kudziyika mchionongeko, ndipo munthu otero akafunsidwa pa tsiku la chimaliziro pa kunyala-nyaza kwake.

8.1. Msilamu aliyense ali ndi udindo otetezeratu zinthu zisadafike powonongeka kapena povuta, ndipo ngati mphamvu yotha kutero ilipo iye nanyala-nyaza ndiyekuti pamenepo walakwira malamuro a Shari'ah ndipo akafunsidwa pa tsiku la chimaliziro.

9.1. Msilamu aliyense adziwe kuti kuwamvera omwe akutilamura (ngakhale atakhala osakhulupirira) ndi kokakamizika, bola ngati zomwe akulamulazo nzosatsutsana ndi malamuro a Shariah. Chomwecho Msilamu adziwe kuti potsatira ndondomeko zimenezi ndiyekuti iye akutsatira malamuro a Shariah mbali zonse. [**Qur'an 4, Ayah 59**].

2) KUIMIKIRA MAPEMPHERO A PAGULU PA ZIFUKWA ZOMVEKA

1.2. Msilamu aliyense adziwe kuti kupemphera pagulu ku Msikiti ndi ntchito yokakamizika kwa amuna otha nsinkhu, ndipo ndi tchimo lalikulu kwa amene akusiya kupemphera pagulu popanda zifukwa zomveka pa Shari'ah.

2.2. Msilamu adziwe kuti malamuro a Shari'ah akuwalola asilamu kuyimikira mapemphero apagulu napemphera kunyumba kwawo ngati pali zifukwa zomveka monga; mvula ya dzaoneni, kudwala, mphempo yowopsya, chimdima chadzaoneni, ngati pali chiwopyezo cha anthu achifwamba ndi achiwembu, ngati pali chiopsezo cha matenda ofalikira ndi zina.

3.2. Msilamu adziwe kuti pali nthawi zina zomwe kuchita mapemphero apagulu kumakhala koletsedwa kwa munthu, ndipo amakakamizidwa kuti apemphere kunyumba kwake. Monga; ngati ali ndi nthenda yomwe angathe kuwapatsira ena, ngati wadya zakudya za fungo loipa lomwe lingathe kuwasawutsa ena monga adyo, anyezi ndi zina, ngati iye sadatsuke mkamwa. Ndi zina ngati zimenezi.

4.2. Msilamu aliyense adziwe kuti Misikiti sikuti ikutsekedwa ayi, koma chomwe chikuimitsidwa apa ndi kupemphera kwa pagulu kwa nthawi yochepa chabe osati mpaka muyaya ayi. Kupemphera kwa pagulu kukuyimitsidwa pa chifukwa chofuna kuteteza miyoyo yathu ndi miyoyo ya ena ku kufalikira kwa mulili omwe watipeza.

5.2. Msilamu adziwe kuti panthawi zimene tapanikizika malamuro a Shari'ah akutilamura kupanga nyumba zathu kukhala misikiti yopemphereramo kufikira mpaka zinthu zitakhala bwino. Allah akuyankhula (pa nkhani ya Mtumiki Musa ndi anthu ake) kuti: '..**ndipo nyumba zanu zipangeni kukhala misikiti**……'. [Qur'an 11, Ayah 87].

6.2. Msilamu asawone ngati malipiro akupemphera kwa pagulu sawapeza chifukwa chakuti wapemphera kunyumba kwake. Akumbukire kuti ngati iye mtima wake uli ofunitsitsa kupemphera pagulu ku msikiti koma akukanika kutero pa zifukwa zokwanira, ndiyekuti Allah akumulipira ngati wapemphera ku msikiti pagulu. Mtumiki (s.a.w) adati: '**ndithu ntchito zimalipidwa (ndikulandiridwa) malingana ndi zitsimikizo zake**'. [Bukhari/Muslim].

3) KHALIDWE LA MSILAMU WENI-WENI NTHAWI YA ZOVUTAYI

1.3. Msilamu weni-weni sachita zinthu mwaumbuli ngati alibe nzeru. Ndipo salola kulumidwa ndi njoka kawiri dzenje pa limodzi.
2.3. Msilamu weni-weni amadziwa kuti kumuopa Allah sikutanthauza kuti iye achite zinthu mopanda nzeru. Koma kumuopa Allah ndiko kugwiritsira ntchito njira zonse zomwe Allah ndi Mtumiki wake walamura ndi kulangiza.
3.3. Msilamu sachita zinthu momuyesa Allah, koma iye amatengapo gawo ndikuchita mbali yake kenako ndikumusiyira Allah kuti amuthandizire.
4.3. Msilamu weni-weni amadziwa kuti Shari'ah imatha kutsogoza kuwuteteza moyo podziwa kuti Deen kuti itheke pakufunika munthu akhale ndi moyo.
5.3. Msilamu weni-weni amalimbikira maduwa ndi kumulilira Allah kuti amufungatire iye ndi asilamu anzake ndi chisomo chake powateteza ku zovuta ngati mulili omwe watigwerawu.
5.4. Msilamu weni-weni amatsatira ndi kuvomera zomwe akulu-akulu a chipembedzo afotokoza kuchokera m'buku la Allah ndi mau a Mtumiki wake (s.a.w).